

# MNENERI WOCHITA MANYAZI



Tsopano Ambuye awonjezere madalitso Ake ku phunziro la:  
*Mneneri Wochita Manyazi.*

<sup>2</sup> Mmawa uno ife tinatengeka kwambiri ndi mneneri yemwe anavala mwinjiro wosiyiridwa. Ndipo ife tikudziwa usikuuno, chikhalireni mu Lemba, m'mawa uno, kuti ife eniake tavala mwinjiro wosiyiridwa. Ife...mwinjiro. Ndipo ine ndiri wokondwa kwambiri kuti iwo ndi mwinjiro wosiyiridwa, pakuti mwinjiro uwu umene ife tikovala tsopano wazindikiridwa kwa Mulungu kuti ndi chirungamo, kudzera mwa Khristu Yesu. Ndipo ife sitikutenga mwinjiro wodyedwa-ndi-njenjete wa theology ya munthu umene wadyedwa ndi njenjete ndi zitete, ndi zina zotero, kumanena kuti, "Masiku a zozizwitsa anapita, ndipo kulibeko chinthu chotero chonga ku—kupezekaponseponse kwa Mzimu Woyera tsopano." Koma ife tikovala mwinjiro wa chirungamo Chake.

<sup>3</sup> [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Osati mwa kuthekera kwathu, koma mu—kuthekera kwa Ambuye wathu Yesu.

<sup>4</sup> Ndipo pamene ine ndizidzafika ku Yorodani, ine ndikufuna ndidzakhale nditavala mwinjiro Wake, ndikudalira mwa Wake. Ndipo mthunzi wawukulu wa chipata womwe waikidwa patsogolo pa ife tonse, wotchedwa "imfa," nthawi iliyonse imene mtima wathu ugunda, ife timapita kugunda kumodzi moyandikira ku mpita waukulu umenewo umene mwamuna aliyense ndi mkazi akuyenera kudzadzutsapo. Ndipo pamene ine ndidzafika pa mpita umenewo, limodzi ndi inu okhulupirira, ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti sindidzapita kumeneko ndi ichi mu mtima mwanga ndi mmalingaliro mwanga, kuti ine ndachita chinachake chachikulu. Ine ndidzapita kumeneko, ndikuvomereza ndi kumadziwa kuti ndine wochimwa, ndi kumadziwa ichi, kuti, ine ndikufuna ndidzadzikutire ndekha mu minjiro ya chirungamo Chake; ndiri ndi umboni uwu, kuti, "Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiukitsiro Chake." Kutu, pomwe Iye adzaitana kuchokera kwa akufa, ine ndikufuna ndidzatzulukire.

<sup>5</sup> Tsopano, chochitika chathu ndi sewero zaikidwa usikuuno kwa mutu wathu, za tsiku lina mu Israeli, limene linali pafupifufupi zaka mahandiredi angapo kudutsa nthā—nthawi ya Eliya. Zokwera ndi zotsika zambiri zinali zitabwera mu ulamuliro wa Israeli. Ndipo tsopano ife tiri pa chochitikacho usikuuno...

<sup>6</sup> M'mawa uno ife tinali pa chochitika cha kumene kunali zotsanzira zachithupithupi zochuluka, m'mene kuti sukulu ya

aneneri inali kumeneko kuphunzira kuti adzakhale aneneri. Ndipo m'mene iwo analiri ophweka, mpaka kuti analephera kuti aimvetse mphamvu ya Mulungu. Iwo ankaganiza kuti mphamvu inamunyamula Eliya m'mwamba ndi kukamponya iye uko pa phiri kwinakwake, ndipo iwo anatumiza gulu lofufuza kuti likamusake iye. Pamene, Elisha ankadziwa, bwino bwino, kuti Mulungu anali atamutenga kupita naye iye ku Ulemerelo. Pakuti, iye anangosowa. Mulungu anali atamutenga iye, ndipo iye anaizemba imfa popita Kwawo kwa Mulungu, pa gareta wa Moto ndi akavalo a Moto. Ndipo kenako ife tinawona kuti maseminare awo ndi ntchito zawo zomwe za theology sizinagwire ntchito. Zinatengera kusankha ndi kuitana kwa Mulungu kuti zipange mneneri wa Mulungu.

<sup>7</sup> Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikumupeza Israeli ali mu chikhalidwe chobwerera m'mbuyo. Israeli anali ndi zokwera ndi zotsika zake. Icho chinali choimira kumene cha mpingo lero. Nthawi zina iwo amakhala pa madenga a nyumba, nthawi inayo iwo amakhala kumusi mu chigwa. Ndi zimene zimatengera kuti zitipangitse ife kuyamikira chinthu chabwino. Pali chomwe iwo amachitcha lamulo losiyantsa.

<sup>8</sup> Munthu wakuda waku Africa sankadziwa konse kuti iye anali wakuda, khungu lake, kufikira iye atamuwona David Livingston. Ndipo iye anati. . . Pamenepo iye anazindikira kuti khungu lake linali lakuda, chifukwa la Livingston linali loyera. Ndi kusiyantsa.

<sup>9</sup> Inu simukanadziwa konse kuyamikira usana ngati inu mukanakhala kuti munalibe usiku. Inu simukanadziwa konse kuyamikira kuwala kwa dzuwa ngati inu mukanakhala kuti munalibe tsiku la mitambo. Inu simukanadziwa konse kuyamikira chirungamo, pokhapokhapo inu mukanakhala ndi kusalungama kwina. Inu simukanadziwa konse kuyamikira thanzi labwino, pokhapokhapo inu mukanakhala ndi thanzi lamatenda, thanzi lina losakhala bwino. Ndi okhawo basi. . .

<sup>10</sup> Ndipo ndicho chifukwa chake ine ndikuganiza kuti ife tidzakayamikira Kumwamba mochuluka kwambiri, chifukwa ife tinayamba takhalapo padziko lapansi. Ndipo ine ndikuganiza lamulo la kusiyantsa. . . Chifukwa chimene ife tikuyamikira Mzimu Woyera kwambiri, usikuuno, ndi chifukwa chakuti ife tinakhala nthawi yaitali mu tchalitchi chimene ankatuza ife kuti kunalibe chinthu choterocho. Chifukwa chimene tikuwuyamikira iwo, usikuuno, chifukwa ife tinakhalapo nayo mbali inayo. Ndipo umo ndi momwe Mulungu wazifunira izo kuti zikhalire, chifukwa anthu Ake akhalapo nazo zokwera ndi zotsika zawo. Inu simungadziwe konse kuyamikira pamwamba pa phiri, pokhapokha ngati inu munakhalapo mu chigwa. Ndipo, chotero, inu simungadziwe konse kuyamikira madzi abwino pokhapokhapo inu mutamwapo madzi ena oyipa

nthawiyina. Ndiyeno inu—inu...Kudutsa njira yonse, ndi lamulo losiyanitsa.

<sup>11</sup> Tsopano, Israeli anali mu chimodzi cha zikhalidwe zake zobwerera m'mbuyo, ndipo ndi chinthu bwanji chimene iwo anali atachita!

<sup>12</sup> Tsopano, Israeli anali anthu osankhidwa, opatulidwa, osankhika, kuti Mulungu anali atamusankha Israeli pa cholinga chinachake chimodzi, kuti magazi a Israeli akhale mzere wa magazi woyeretsetsa, pakuti kuchokera mu mndandanda umenewo wa m'badwo unali woti adzatulukako Mesiya Iyemwini.

<sup>13</sup> Monse kudutsa mu Chipangano Chakale, Mulungu amawonekera mwa munthu. Mulungu anawonekera mwa Abrahamu, ngati wokhulupirira wa chikhulupiriro. Mulungu anawonekera mwa Davide, ngati mfumu. Iye anawonekera mwa Yosefe, ngati chirungamo. Iye anawonekera mwa Mose, ngati mneneri, wansembe, wopereka-lamulo. Iye amawonekera kutsika kudutsa mu mibadwo, mwa mneneri. Iye nthawizonse amadzipangitsa Yekha kudziwika mwa anthu, mwa kagawo, kudzera mwa mneneri, mfumu, wansembe, wopereka-lamulo, zina zotero. Koma, mwa Khristu, Iye anadzakhala mwa Iye, chidzalo cha Umulungu mthupi, ndi kumadziwa kuti Mzimu uwu ukuyenera pomaliza udzapeze malo odzapumulapo. Pa Eliya, iye anali mwamuna wa chirungamo cha Mulungu. Iye anabangula chirungamo cha Mulungu. Ndipo, Mose, iye anali wopereka-lamulo, kuti inu munyindirire pothera kapena mutuluka. Mu zinthu zonse izi, Mulungu amaimiridwa. Koma pamene Iye anadzabwera kwa Khristu, Iye anali wangwirowo, chidzalo chonse cha Umulungu mthupi chinadzakhala mwa Khristu.

<sup>14</sup> Ndipo Mulungu anadziimirira Iyemwini kamodzi mu chidzalo, isanafike nthawiyo. Mu Bukhu la Genesis, mu dongosolo la Melkizedeki, “Amene analibe bambo, analibe amayi; analibe chiyambi cha masiku, kapena mathelo a zaka, kapena mathelo a moyo.” Ndipo Iye anali Wansembe, Mfumu yaku Salemu, wansembe wa Mulungu, wa Mulungu wammwambamwambayo, Amene anali wopanda chiyambi kapena wopanda mapeto. Iye sanali winanso koma chowonetseratu cha Ambuye Yesu Khristu. Chifukwa, Iye anali Mfumu ya Salemu, yemwe ali Mfumu ya Mtendere, yemwe ali Mfumu ya Yerusalemu. Ndipo Iye anali mu chowonetseratu. Ngakhale mbadwa Abrahamu anapereka chakhumi kwa Iye. Iye anali chowonetseratu cha kubwera kwa Ambuye Yesu. Melkizedeki yemweyo anadzakumana ndi Abrahamu kuzidikha uko kusanachitike kuwonongeka kwa Sodomu ndi Gomorrah. Ndipo—ndipo Iye anadzakumana naye iye atathana naye Sodomu ndi Gomorrah, pamene Abrahamu anampatsa Iye

zakhumi za zofunkha zonse zimene iye anatenga kuchokera kwa mfumu.

<sup>15</sup> Zinthu zonse izi zikuchitiridwa mthunzi, kuimiridwa mpaka kwa Khristu. Ndipo tsopano, mthunzi yonse ya oyera a Chipangano Chakale, zokwera ndi zotsika zawo, zinali mthunzi ndi choimira, ndi zitsanzo za ife lero.

<sup>16</sup> Tsopano, ife tikupeza kuti Israeli sanali woti adzisakanizana chikwati. Chikwati chawo chinali choti chidzikhala pakati pa wina ndi mzake, osati kuti m'Israeli wina azikwatira nkomwe Wamitundu, koma anali woti mzere wamagazi wawo udzikhala woyera. Ndipo ngakhale kufikira tsiku lino, ine ndikukhulupirira kuti mzere wamagazi Wachiyuda ndiwo wamagazi woyeretsetsa—mzere wamagazi pa nkhope ya dziko lapansi lero, ndi Myuda. Iwo akumuyembekezerabe Mesiya ameneyo. Koma, Iye . . . Iye tikudziwa kuti Iye anabwera kale; ndipo maso awo anachititsidwa khungu, kuti ife tidzakhoze kukhala ndi mwayi wa kulapa kudzera mwa Khristu.

<sup>17</sup> Tsopano, mu nthawi ya ulamuliro wa Ezra, ana a Israeli anali atabwerera m'mbuyo. Iwo anali atatuluka ndipo anakatenga akazi achiMoabu, ndipo anali atakatenga akazi achiAmori, Aperezi, ndi ambiri a mafuko enawo. Ndipo sikuti anangowakwatira kokha iwo, koma anali akuchita chiwerewere pakati pawo, chidetso, ndi kuyipitsa mzere wamagazi womwewo, umene uli mzere wa moyo.

<sup>18</sup> Ndipo ndi chithunzi bwanji icho lero cha mipingo yathu, m'mene iyo ikupasukira kuchoka ku mzere wamalire wachikale umene Mulungu anawuyalira mpingo. Malangizo amene ife tinati tidzikhallira nawo moyo, mpingo ukuchita nawo chiwerewere ndi dziko. Iwo watuluka wapita mu dziko, ndipo wayamba kuchita zibwana mdziko.

<sup>19</sup> Tsopano, izi zinali zitamuchititsa manyazi mneneriyo kwambiri, mpaka, pamene iye anadzabwera pamaso pa Mulungu, iye anachita manyazi pa nkhope yake. Poyamba pamene iye anamva za izo, ndipo iye nawona ku—kuvunda khalidwe kwa anthu ake, izo zinamupweteka iye moyipa kwambiri mpaka iye anakhala pansu ndipo anazidzoza iyemwini, anamwetulapo tsitsi lake ndi ndevu zake, ndipo anali wopsyinjika-mumtima pamaso pa Ambuye, mu pemphero. Kenako pamene nsembe yamadzulo inkaperekedwa, iye anapita mu kachisi ndipo anakagwa pa maondo ake ndipo anachita manyazi pamaso pa Mulungu, chifukwa cha machimo a anthuwo.

<sup>20</sup> Tsopano, iye sanachite manyazi chifukwa cha msewu wofiira wa dera la uhulelo. Iye sanachite manyazi chifukwa cha okumwa mwauchidakhwa mu mphanga la gehenalo, ngakhale izo zinali zoipa. Koma, iye anachita manyazi chifukwa cha tchimo la osankhidwa.

21 Ndipo chimene ife tikusowa lero ndi aneneri ena ambiri okhala ndi Mulungu mokwanira mu mtima mwawo kuti azichita manyazi Pamaso pa Mulungu, chifukwa cha machimo a anthu amene amadzitcha iwoeni kuti anthu a Mulungu ndi kumachita m'mene iwo akuchitiramu. Ife tabweretsa chonyazitsa bwanji ku malo ano! Makhalidwe a anthu athu. . .

22 Ili si phunziro lophweka kuyankhulapo. Ine ndikanakhoza kuganizira za zinthu zambiri zomwe zinali zophweka kuyankhulapo. Koma, m'bale, ngati wina sangaimirire mu tsiku lochimwa ili, lachigololo limene ife tikukhalamo, ndi kutchula manga manga ake, kodi pachitika chiyani? Winawake akuyenera kuti achiyankhule chinthucho. Winawake akuyenera kuti achiike icho pamaso pa anthu.

Mwinamwake Ezra sanafune kuti achite zimenezo, koma izo zinali mu mtima mwake.

23 Ndipo pamene inu mumuwona wantchito wa Mulungu atafika powona mtima kwambiri mpaka nkukhala pa nkhope yake ndi manja ake m'mwamba, akupemphera kwa Mulungu, ndi kuchita manyazi chifukwa cha kusaeruzika kwa anthu, zikatero inu muwona chitsitsimutso chitayambika. Munthu sangakhale Pamaso pa Mulungu, mpingo sungakhale Pamaso pa Mulungu, pansu pa kulapa, pokhapokhapo Mzimu Woyera utatsika ndi kudzapereka kudzodza ndi mphamvu yoti iyambitse kuyenda kwa Mulungu m'menemo pakati pa anthu amenewo. Zikungoyenera kutero!

24 Mundisonyeze ine mwamuna. Mundisonyeze ine Calvin wina, Knox, Finney, Sankey, kapena aliyense wa iwo amene amamverera kupsyinjika chifukwa cha anthu, omwe angagone pankhope zawo ndi kulira ndi kupemphera pamaso pa Mulungu. Titumizireni ife John Smith wa Baptist church wina, yemwe anapemphera utali wa usiku wonse chifukwa cha kusaeruzika kwa anthu, kufikira maso ake anatupa nkutsekeka m'mawa wotsatirawo, chifukwa cholira, mpaka mkazi wake amamutsogolera iye ku tebulo ndi kukamudyetsa kadzutsa wake ndi supuni. Mundisonyeze ine John Wesley winanso, chitsulo chotentha chofumulidwa ku moto, ine ndikuwonetsani inu chitsitsimutso.

25 Chomwe iwo akuchita lero, ife tikuzisisita izo pa nsana. Ife tikudzitcha izo *ichi* ndi *icho*, ndi chitsitsimutso, pamene palibepo chitsitsimutso kwa izo. Uko nkulondola. Pali kutakasa kwa kutentheka kwa chipembedzo pakati pa anthu, koma palibepo chitsitsimutso.

26 Iwo anali ndi gulu la chipembedzo mu tsiku limenelo. Iwo anali ndi kutakasa mu tsiku limenelo, koma iwo ankasowa chitsitsimutso.

27 Chifukwa chiyani, m'bale wanga wokonedwa ndi mlongo, zikhalidwe za fuko lino zafika potsikitsitsa kwambiri mpaka

zingapangitse galu kuchita manyazi. Izo zingapangitse imbwa kuchita manyazi ngati iyo ingathe kutero, kupanda khalidwe kwa anthu athu! Anthu, ngakhale zaka zapitazo, zinthu zimene ife tiri nazo, fu—fukoli lachita, zinthu zimene anthu achita! Zonsezo ndi kusowejera kwa mphero.

<sup>28</sup> Mpingo umene unyakonda ku, sunkakhulupirira mu makanema, iwo samawaloleza ana awo kupita ku makanema. Iwo amakaniza kanema. Ndipo, lero, bwanji iwo mpaka ali ndi...Iwo ankakhala ndi kanema mnyumba zawo zomwe. Nyumba iliyonse ili ndi televizioni.

<sup>29</sup> Mu malo omwe iwo ankaganiza kunali kolakwika kuti azikamwerako mowa, mmalo amene iwo ankaganiza...John Barleycorn, iye anali mnyamata wovunda bwanji. Lero, sikisite peresenti ya otchedwa Akhristu amamwa kachakumwa ka mchezo pafupifupi kamodzi pa chaka. Kenako iwo amadzakhala ndi chisangalalo chachikulu, chamu Khristmasi, pamene iwo amakhala ndi chikondwerero chawo. Chifukwa, iwo atenga maphunziro kuti alowe m'malo a chipulumutso. Iwo sangachite konse zimenezo.

<sup>30</sup> Chimene ife tikusowa ndi chitsitsimutso. Ife timavala zikhakha zachimanga, timazivula izo; chikhakhachina cha chimanga, kuchivula icho, ndipo nkumapezabe kuti kupwetekako kukadalipobe pamenepo. Chimene ife tikusowa lero si kusinthika kwa wamba, si kuyankhula kwa luntha. Chimene ife tikusowa lero ndi kachitidwe-kachikale, kupatsidwa Magazi kotumizidwa ndi Mulungu kochokera Kumwamba. Zikhakha zachimanga sizingachite ubwino uliwonse. Ife tikusowa magazi. Ife tikusowejera kupatsidwa Magazi. Ife tikusowejera kuti tibwerere ku Uthenga wakachitidwe kachikale umene umaitanira ku kulapa pamaso pa Mulungu. Ndipo osati kuvomereza kwa mmaso mowuma, kogwirana chanza; koma chitsitsimutso chotumizidwa ndi Mulungu, cha Mzimu Woyera chokhala nako kutsuka kwa Magazi a Ambuye Yesu Khristu kulowa mu mtima uliwonse wa munthu. Ife tikusowa chitsitsimutso chiyambire mu Tchalitchi, ndi kudzasesa fuko lonselo. Ife tifa, tiwonongeka, titha, tikapanda kukhala ndi chitsitsimutso cha mtundu umenewo.

<sup>31</sup> Ndine wodwala kwambiri ndi wotopa chifukwa chowona tizitsitsimutso tating'ono ta Hollywood, totchedwa choncho, timene anthu amabwera ndi kudzatakasika kwa maora angapo, ndi, kapena tsiku kapena awiri, kapena sabata kapena awiri, ndi kuchokapo ndipo ndizo zonse za izo. M'bale, inu mukhoza kukhala mu...kugwiritsidwapo ntchito ndi chitsitsimutso. Inu mukhoza kukhala ndi kutengeka. Inu mukhoza kukhala ndi zolinga zabwino. Zinthu zonsezo ndi zabwino, koma ife sitikuzisowa zimenezo lero.

<sup>32</sup> Ife tikusowa ubatizo wa Mzimu Woyera, kuti usinthe zotengekazo, ndi luntha, ndi kawonedwe, zizolowezi, moyo wa anthu, ndi kuzibwezeretsanso izo pa msewu wolondola kachiwiri. Kunja kwa kupatsidwa Magazi ochokera ku Kalvare, kukonzanso kwathu konse sikungachite ubwino uliwonse nkomwe.

<sup>33</sup> Ife sitikusowa U.N. Ife tiri nayo U.N. kumeneko, ndipo kodi iwo amachita chiyani? Dzina la Mulungu silitchulidwa nkomwe. Iwo amawopa kuti alitchule Ilo. Zinafunsidwapo nthawiina, ndi gulu la azibusu, “Nchifukwa chiyani iwo sanakhale ndi pemphero?” Iwo anati, “Zikhoza kumulakwira wina, mmodzi wa enawo amene sakhulupirira Mulungu.”

<sup>34</sup> Oh, chimene ife tikusowa ndi chitsitsimutso. Sizipanga kusiyana kulikonse kuti zimulakwira ndani, ife tikuyenera kuti tizilalikira Uthenga ndi kulola manga manga athu agwire ntchito. Kulondola. Ine sindingakupatseni inu khobiri pa dongosolo lililonse limene lamusiya Mulungu kunja kwake, kaya ndi U.N., kapena big-four, chirichonse chimene izo chingakhale.

<sup>35</sup> Kufikira fuko lino litadzuka pa malowo, akuti tikufa opanda Magazi a Ambuye Yesu Khristu; kufikira anthu pawokha atadzuka ku—choyambitsa chake, kuti ife tikufa! Chifukwa chimene ife tikufera, ndi chifukwa chosowa chapachiyambi, njirayo, yankho, machiritso amene Mulungu anatipatsa ife pa Kalvare.

<sup>36</sup> Ndi zosadabwitsa izo zimampangitsa munthu kuchita manyazi! Ndi zosadabwitsa! Mlaliki weniweni, woona amayang’ana pa gulu lake ndipo amayesetsa kuti awatsogolere iwo pamaso pa mpando wachifumu wa Mulungu. Ndipo akakachezera makomo awo, ndi kuwapeza iwo akusuta ndudu, akunena nthabwala zonyansa kwa wina ndi mzake, zisangalalo kuseri kwanyumba, ndi maphwando amowa; kumayendayenda pa misewu, akazi awo aang’ono, ndi a mzaka-zapakati, ndi zina zotero, ndipo ngakhale agogo aakazi atavala akabudula aang’ono. Mayi ali kunja uko mu msewu ndi khanda lake pa nkono wake umodzi, atavala mwachiwerewere ndithu kuti akope tcheru la chidakwa chirichonse chomwe chiti chiyende mumsewu; ndipo nkumadzitcha okha Mkhristu. Izo zingampangitse munthu wa Mulungu woona aliyense kuchita manyazi, kuti amubweretse munthu woteroyo Pamaso pa Mulungu. Kulondola!

<sup>37</sup> Ndipo kujowina tchalitchi kwathu konseku ndi kupeza kagulu kabwinoko, zafika pa zamkhutu, ndipo izo zinatero mu tsiku limenelo ndipo izo zitero apa. Tibwezeretseni ife kwa Mulungu, osati ndi maphunziro, osati ndi jakiseni wa kukonzanso kwa zipembedzo, osati mu mtundu wina wa theology yopangidwa ndi munthu. Koma ubatizo wa kachitidwe kachikale ka Mzimu Woyera wotumizidwa

kuchokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba, mu chokuchitikira cha chipentekosite chowotcha kunyengezera. Ndi kubwezeretsamo mmenemo ngale imene Mulungu analinga kuti idzakhale mkatimo, ya mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu. Kufikira ife titachita zimenezo, abale ndi alongo, ife tidzikhalabe ndi akazi ometa-tsitsi, odziphoda, owoneka-mwachiwerewere; ndi amuna akumwa, osuta, ndi kumadzitchula iwoeni Akhristu; chifukwa iwo sakudziwa ubwino uliwonse. Mu mtima mwawo, muzu kumene wa chithupithupi ukukhala m'menemo, ndipo ife tikusowekera kuyeretsa kwa mpingo, kuchokera kumusi mpaka ku guwa. Amen. Ndipo uko nkulondola.

<sup>38</sup> Chomwe ife tikusowa lero ndi aneneri ena ochita manyazi. Mulungu...Nthawizina anthu amabwera mu mzere wa pemphero, kuti adzapemphereredwe, amawoneka ngati akupita kunyumba ya mbiri yoyipa. Uko nkulondola. Kubwera kuti adzamupemphe Mulungu chinachake, ndipo nkumawoneka ngati Yezebeli. Chimene ife tikusowa lero ndi kuyeretsa mnyumba ndi kutenthetsa mitima, kwa aneneri a Mulungu amene angaime pa guwa ndi kuchitchula poyera chinthucho, ndi kunena chomwe chiri choona ndi chomwe chiri cholakwika; ndi kulalikira Uthenga mopanda kunyengerera, kufikira ochimwa kugwera pansu, ndi kumalira mpaka Mulungu atatumiza Mzimu Woyera kuti udzayeretse moyo wawo. Amen. Ife tikudziwa uko nkulondola. Uko nkulondola.

<sup>39</sup> Ine ndinalalikira kuno osati kale kwambiri ndipo ndinati mkazi aliyense mu mzinda uno anali wolakwa, mwa njira imodzi kapena imzake, za chigololo. Iwo ali. Akazi amapita mtawuni uko ndipo iwo sakhoza nkomwe kuti agule dresi, pokhapokha likhale ngati kuti iwo achita kupunguliridwa mwa ilo. Ine sindiri pano kuti...Ichi ndi tchalitchi changa changa. Ine ndiri ndi ufulu wolalikira chimene Mzimu Woyera ukundiiza ine kuti ndichite. Kulondola.

<sup>40</sup> Ndiloleni ine ndikuuzeni inu. Ine sindiri kukutsutsani inu, mlongo wanga. Koma kodi Mzimu Woyera sukuphunzitsani inu mosiyana? Ngati iwo sutero, pepani inu simunalandire Mzimu Woyera. Uko nkulondola. Mzimu Woyera si "kufuula." Mzimu Woyera si "kuvina mu Mzimu." Mzimu Woyera si "kuyankhula mmalirime." Mzimu Woyera ndi chirungamo. Mulungu, tipatseni ife chitsitsimutso cha Mzimu Woyera cha chirungamo chotumizidwa ndi Mulungu.

<sup>41</sup> Kodi inu simukuzindikira kuti pamene inu mudziveka nokha monga choncho ndi kumayenda mu msewu, ndipo amuna akayang'ana pa inu mwanjira yolakwika, kuti pa Chiweruzo...Inu mukhoza kukhala wangwiro ngati kakombo, pamaso pa amuna anu. Koma, pa Chiweruzo, inu mudzakhala wolakwa chifukwa chochita chigololo ndi njonda imene inu munadziperekako inueni.



42 Ndi zosadabwitsa Izo zikhoza kumupangitsa munthu kuchita manyazi! Ndi zosadabwitsa! Kodi izo zimachita chiyani kwa Mulungu? Pamene, Baibulo linati, pachiyambi, kuti, “Zinamukwiya Iye, kuti Iye anampanga munthu.” Izo zinakwiya mtima wa Mulungu, pamene Iye anayang’ana pa iwo mmasiku chisanachitike chiwonongeko cha chigumula, kuti Iye anampanga munthu. Chinachitika ndi chiyani? “Ana aamuna a Mulungu anayang’ana pa ana aakazi aanthu kuti anali okongola.” Uko kunali kupotoza. Uko kunali kusakaniza kwa kugonana. Chinali chinthu chimenecho chimene chinawachotsa ana a Mulungu mmunda wa Edeni. Chinali chinthu chimenecho chimene chinapangitsa chiweruzo cha Mulungu, kuti abweretse mtendere pa dziko lapansi. Chinali chinthu chimenecho chimene chinapangitsa kuti iwo awonongeke. Kunali kusakanizikana komweko, pakati pa akazi ndi amuna, kumene kunapangitsa Sodomu ndi Gomorrah kumira pansu pa Nyanja Yakufa.

43 Zinanenedwa ndi aneneri. Zinanenedwa ndi Ambuye Yesu, kuti, “Monga zinali mmasiku amenewo, chomwechonso iwo zidzakhala kusanati Kudza kwa Mwana wa Mulungu.” Ize timayang’ana lero, ndipo timawona kuti mpingo ukutenga kachitidwe kake osati kuchokera mu Baibulo, kuchokera kwa Rute ndi Naomi, ndi kuchokera kwa Sarah ndi iwo a mu Baibulo. Koma iwo akutsanzira, ngakhale akazi a mu mpingo, za ku Hollywood ndi zikoka kumene za mdierekezi.

44 Ndipo momwe kuti anthu athu, amene amadzitcha okha Akhristu, amapita kunja uko ndipo amakatengera njira za munthu woyipa izi. Ma rekodi awa a Elvis Presley, kaya dzina lake ndi litilo, mmodzi wa wosocheretsedwa kwambiri, anthu odzadzidwa ndi mdierekezi amene ine ndinayamba ndawamvapo mmoyo wanga. Arthur Godfrey ndi zonga zimenezo, ndi kumamvetsera zamkutu za mtundu umenewo pa mawailesi anu; ndi kumakana kumvera ulaliki wa Uthenga ukulalikidwa, ndi Baibulo. Mulungu akuchitireni chifundo inu. Ndi mtundu wanji wa mzimu umene ife tiri nawo pakati pathu? Uko ndi kulondola.

45 Ndi zosadabwitsa mneneri wa Mulungu anachita manyazi pamaso pa—pa Ambuye. Iye anadziwa kuti uko kunali kusalungama. Ndipo iye anaimirira ndipo anachonderera mlanduwo, ndipo anati kwa Mulungu, “Ndife osalungama.”

46 Ndipo ife tiri, abwenzi, kufikira ife titabwerera ku malo aja a kupatsidwa Magazi. Musiye kumayesera kuvala zikhakha. Musiye kumayesera kudzola mafuta ena. Machiritso sangakhoze kubwera pokhapokha mpita wa magaziwo utakhala wabwino.

47 Ndi chifukwa chake anthu ali ndi nthenda ya shuga. Ngati wina atadzicheka yekha, apo mwinamwake sipangapole. Chifukwa chiyani? Chifukwa zidutswa za magazi zofiira zenizenizo zinadyeka.

48 Ndipo mpingo wonse ukudwala nthenda ya shuga. Ndipo kuchekeka kwakung'ono kulikonse kumene kungabwerepo, mmalo momayendabe, inu mumatsutsula pa iko. Iko sikungapole. Kudzikonda, dyera, kupanda makhalidwe, china chirichonsecho chimene chiri pa kalendara ya Mulungu ya “ntchito-zoipa,” mpingo ukutenga zizolowezi zimenezo. Amuna kumwa, kusuta, kunena nthabwala zonyansa. Akazi kumeta tsitsi lawo, kudzipentapenta, kumachita mitundu yonse ya zinthu, kumadziveka okha mopanda makhalidwe kuti akakumane nawo anthu. Zinthu zonsezi ndi chifukwa cha kusowa Magazi a Ambuye Yesu Khristu kuti atiyeretse ife ku kusalungama konse. Amen. Zimenezo zikhoza kuwoneka zolimba. Ndithudi, ndi zolimba, koma ndi Choonadi.

49 Ngati ife sitigeyapo ziweruzo za Mulungu wamphamvuzonse, inu mudzagwidwa limodzi la masiku awa mu kuphulika kwa atomiki kuno, kumene kuti kudzatumize moyo uliwonse kupita ku Muyaya, kuti ukakumane ndi Mulungu amene ati adzangozindikira Magazi a Mwana Wake, Khristu Yesu. Ine ndikufuna ndikuwoneni inu mukubwera pansu pa Magazi. Langizo langa, kwa inu, ndi kuti mukonzane ndi Mulungu. Langizo langa kwa inu.

50 Chabwino, bwanji ife sitikukhala ndi chikhulupiro? Bwanji ife sitikukhala ndi machiritso aakulu kuposa omwe ife tiri nawo? Bwanji ife sitikudzipeza tokha omangika bwino? Ndi chifukwa chakuti ife tikuvala zikhakha za chimanga; chifukwa chakuti tikuvala zomata; tikuvala zidutswa za tepi. Ife tikuyesera kuti tidzichiphimba chinthucho, m'malo monena kuti ife tikusowa kupatsidwa. Ife tiribe Magazi. Ife tiribe Khristu. Inu musazipusitse nokha.

51 Musalole mdierekezi azikusisitani inu paphewa, kumati, “Chabwino, ine ndimapita ku tchalitchi.”

52 Mdierekezi amatero, nayenso. Uko nkulondola. Iye ndithudi anatero; anabwera kwa Mulungu, anapita ku tchalitchi Kumwamba; anabwera pamaso pa Mpandowachifumu wa Mulungu, ndi ana aamuna a Mulungu, anakhala pansu limodzi nawo, anakhala ndi zoyankhulana ndi Mulungu. Iye anati, “Iwe wakhala ulikuti?”

53 Anati, “Kuyendayenda uku ndi uko, chokwera-ndi-chotsika, pa dziko lapansi.” Ndiko kumene iye anakhala ali.

54 Koteru, mdierekezi amapita ku tchalitchi. Mdierekezi ndi wa mtchalitchi. Mdierekezi amachita ngati Mkhristu. Iye ndi wonyenga. Ndipo ngati Iye akanati asamachite ngati Mkhristu ndi kumachita ngati tchalitchi, iye sibwenzi ali wonyenga; panalibe munthu amene akananyengedwa. Chinthu chokhacho, kusi yana kwake ndi monga kuda ndi kuyera. Ndi zotsutsana china kwa chimzake. Koma Iye... Baibulo linati, “Izo zidzakhala zofanana kwambiri mwakuti zikanati

zidzanyenge Osankhidwa kumene ngati nkotheke,” mzimu umenewo mu tsiku lomaliza. Abwenzi, tiri pamenepo.

<sup>55</sup> Ndi nthawi ya aneneri a Mulungu, oh, m’bale, ya alaliki, ngati inu munganene izo, kudutsa fukoli, kuti agwe pa nkhope zawo.

<sup>56</sup> Bwanji, ngakhale, pali mipingo ya Baptist naintini milioni. . . Ya Baptist naintini milioni, kani, mu America; ya Methodist satini milioni; ya Lutera leveni milioni; ya Chiprebyteria teni milioni. Chifundo, taganizani za zimenezo! Ndipo nthawizonse amakhala ku masewero a mpira, kukasangalala. Ndipo Lachitatu usiku, ndipo nthawizina Lamlungu usiku, amakhala pakhomo kuti azimvetsera televizioni ndi wailesi, za tizibakera tatifupi takale ndi nthabwala zimene amazitenga kuchokera ku Hollywood. Moyo wanu ukugudubuzika pa zinthu za mtundu umenewo.

<sup>57</sup> Pamene, inu mumayenera kukhala ndi Baibulo lanu kunja uko kwina kwake, mutakhala pamaso pa Mulungu, muli pa mawondo anu, mukupempherera machimo a dzikoli.

<sup>58</sup> Ndipo ndine wolakwa limodzi nanu. Ine ndapanga lingaliro langa. Mothandizidwa ndi chisomo cha Mulungu, ngati Mulungu wathu ati andipatse ine mphamvu kuti ndikachite zimenezo, ine ndatsimikiza kuti ndikanikizira kupita ku malo a maitanidwe a pamwamba mwa Khristu Yesu, kufikira imfa idzandimasule ine. Mulungu mukhale mthandizi wanga kuti ndichite chomwecho! “Ndithandizeni ine,” ndiro pemphero langa. Powona ntchitozi, ndi powona zinthu zimene ine ndaziwona ndi zimene inu mwaziwona, ndi kumatsalira m’mbuyo, ndi kukhala wosowa magazi mwauzimu.

<sup>59</sup> Ndipo kachisi uyu yemwe ali wodziwika kudutsa dziko lonse, kamalo ka mabuloko a konkire kakang’ono aka kamene kali pa ngodya, Mulungu wakukwezerani inu m’mwamba pamaso pa fuko. Kulondola.

<sup>60</sup> Ine ndikuganiza za chimene Davide, usiku wina, pamene iye anati, “Pano ine ndiri, ndikukhala mu nyumba ya nkunguza, ndipo likasa la Mulungu wanga likukhala mu hema.” Iye anati, “Ine ndimumangira Iye nyumba.”

<sup>61</sup> Natani, mneneriyo, anati, “Uchite zonse zimene ziri mu mtima mwako, chifukwa Mulungu ali ndi iwe.”

<sup>62</sup> Usiku umenewo, Mulungu anawonekera kwa Natani ndipo anati, “Da- . . . Pita ukamuze Davide, ‘Iwe unali ndani, Davide? Iwe unali. . . Ine ndinakutenga iwe kuchokera ku chisa cha nkhosa, ukuweta nkhosa. Ndipo Ine ndinakupangira iwe dzina lalikulu, monga amuna aakulu a fuko.”

<sup>63</sup> Anali ndani mu kachisi wamng’ono wakhala apayu? Kokokoloka kakale kakang’ono, kenakake kokankhidwira panja kakukhala pa ngodya ya Eighth ndi Penn Street, mpaka

Jeffersonville siimadziwa nkomwe pamene iko kanali, ndi anthu omwe amabwera kuno. Ndipo lero, Mulungu, mwa chifundo Chake, wakukwezerani inu mmwamba ndipo wakupangani inu anthu opambana. Bombay, India amadziwa kumene kuli kachisi uyu. Durban amakudziwani inu; mafuko ena onse awa. Africa amadziwa komwe malo awa ali; India, Germany, England, Finland, Sweden, Europe, Asia, iwo onse, kumusi uko mu zisumbu za Thailand, ndi kumusi uko, iwo amadziwa zonse za iye. Ndipo Mulungu watipanga ife kukhala chitsanzo kwa anthu. Ndipo kuganiza, ndiye, Mulungu atatha kuchita zimenezo, ndipo ife nkutembenukapo ndi kumawayawaya mu zinthu za mdziko, ndi kukhala osowa magazi auzimu kwambiri. Bwanji, ife tikuyenera kukhala nyumba yowunikira imene yaikidwa pa phiri, kandulo imene siingakhoze kubisidwa. O Mulungu! Ndine wochimwa chimodzimodzi ndi ena nonse a inu.

<sup>64</sup> Chimene ine ndikutanthauza, ine ndikufuna—ine ndikufuna kulapa kwa kachitidwe-kachikale, kotumizidwa ndi Mulungu, ndi kuitaniranso kwa Mulungu, kuti pamene amuna ndi akazi ayenda kulowa pakomo limenelo, pa ndodo, iwo azitulukamo opanda izo. Pamene wakhungu atsogoleredwa pa khomo apo, iwo azituluka akupenya. Pamene wogontha alowa aliwogontha, iwo adzatuluke akumva. Pamene ochimwa alowa, akuda ndi amwaye ndi tchimo, adzatuluke, atatsukidwa m'Magazi a Mwanawankhosa. Kodi ife sitingathe kuchita zimenezo? Mulungu anaitana Israeli ndipo anawapanga iwo chitsanzo. Mulungu anaitana ife ndipo watipanga chitsanzo, koma ife talekerera pa Mulungu, ndipo izo zikutichititsa ife manyazi mu Kukhalapo kwa Mulungu.

<sup>65</sup> Kuganiza za, zinthu zimene Iye watichitira ife! M'mene Iye watikwezera ife pamwamba kuchokera ku chisakasa cha nkhosa! M'mene Iye watipangira ife kudziwika, konsekonse pa dziko lapansi! M'mene Iye watichitira ife chinthu chachikulu! Ndipo, komabe, ife timawayawanya, ndi kumachita ukamberembere pamenepo ndi kumapita, ndipo ife sitikuwoneka kuti tiri owonamtima. Ife sitikumakhalanso ndi pemphero nkomwe, ndipo zinthuzo basi, mwakuti, sizikuyenda bwino. Ndipo ife tikumayesera kuika timaprogramu tating'ono, zikhakha zachimanga, kuti titontholetse ululuwo. Inu simungathe kutontholetsa ululu kufikira inu mutatengeramo, Magazi abwino okhuthala m'menemo kuti achiritse chinthucho. Kulondola!

<sup>66</sup> Inu mukadula chikundu chakale, ndiye inu mudzitengera nokha matenda a shuga, ndipo izo zingadulitse phazi lanu. Musamayesere kuti muchichotse *ichi*, ndi kuchilambalala *ichi*, ndi kucheka chikhakha cha chimanga pa *ichi*.

<sup>67</sup> Koma chinthu choti muzichita ndi kubwera molunjika pamaso pa Mulungu, ndi kuti, "Mulungu, ine ndikusowa magazi, ndipo ine ndikufuna Magazi Anu kuti anditsuke ine kundichotsa

ku tchimo langa lonse.” Ndiro pemphero langa, ndikudalira kuti ndiro lanunso.

<sup>68</sup> Taganizani za zinthu izi, mzanga. Limodzi la masiku awa; izo ziyenera basi kuti zidzachitika kuwala kwa tsiku kusanabwere m’ mawa, monga izo ziti zidzachitikire zaka fifite kuchokera lero. Bomba limodzi la ndege, limodzi la mabomba a cobalt kapena haidrojini akhoza. . . Fuko lonseli liri tcheru.

<sup>69</sup> Inu munaziwona izo mu pepala tsiku lina pamene iwo akufunsira kwa sayansi, pentagoni, iyankhe za zimbale zowuluka. Iyo siinali nkhabakamwa. Izo sichinachake chimene iyo inangolingalira. Izo zinali zenizeni. Izo zinali luntha. Izo zinauluka mu kupangidwa kwa nkhondo. Iwo akhoza kuziimitsa. Iwo akhoza kuziyambitsa. Iwo akhoza kuziimitsa. Iwo akhoza kuziwiwusa. Izo zinali luntha. Iwo akudziwa izo. Anthu anaseka. Iwo anati, “Zimbale zouluka?” anaziseleula izo.

<sup>70</sup> Koma inu mukudziwa chimene ine ndikuganiza? Yesu anati, Iye asanabwere, kudzakhala zizindikiro Mmwamba umo. Kodi inu munazindikira? Iye asanayambe, kuwononga Sodomu ndi Gomorrah chifukwa cha za chiwerewere zawo, Iye anatomiza Angelo kumeneko kuti akafufuze izo. Angelo abwera pa dziko lapansi zaka zochepe zapitazi. Iwo akhala akuwonedwa pakati pa anthu; ine ndikutanthauza, anthu otsukidwa ndi Magazi omwe amadziwa izo. Iwo mpaka amaimirira ndi kujambulitsa chithunzi. Uko nkulondola. Zinthu zaungelo zadzatichezera, kuwatengera mawu kubwerera nawonso kwa Atate, kuti tchimo launjikika mpaka nyenyezi zikulephera kuwala. [M’ bale Branham akugogoda pa guwa kasanu—Mkonzi.] Mwezi. . . Dziko lonse likudzandima ngati munthu woledzera akamabwera usiku. Kulondola.

<sup>71</sup> Tchimo pakati pa Akhristu, pakati pa Osankhidwa! Iwo agulitsa maufulu awo obadwa, chifukwa cha kutchuka. Mtumiki wasinthanitsa Uthenga ndi phwando wamba. Iye wasinthanitsa Uthenga wachikale wotsukidwa ndi Magazi ndi zaluntha za anthu, kuti azilalikira luntha, kuyankhula za anthu, ndi kusagwiritsa bwino ntchito Uthenga. Ambiri a iwo atuluka apita mminda, kukalalikira, ndipo akuwugwiritsa ntchito Uthenga kwa phindu lawo lawo, kuti akapange ndalama. Ambiri a iwo ali ndi nyumba zazikulu ndi magalimoto, ndi zinthu zomwe iwo sakanakhoza kukhala nazo, phindu lawolawo. Osati onse; ndine wothokoza kuti alipobe wotsalira.

<sup>72</sup> Mu masiku a Ezra, pamene Ezra anayamba kulira, ndi kuitana ndi kudzudzula tchimo, inu mukudziwa chimene chinachitika? Osankhidwa onse, amene ankadalira Mulungu, anasonkhana momuzungulira iye.

<sup>73</sup> Chimene ife tikusowa lero ndi amuna ndi akazi. . . Alaliki anu akulalikira, mipingo imeneyo, ndi kulitchula tchimo “tchimo,” ndi kulidzudzula ilo, anthu enieni a Mulungu

angasonkhanire mokuzungulirani inu, ndi kukhala ndi inu. Uko nkulondola. Ndi nthawi yoti tidzizitchula, ndi kunena chenicheni ndi chiti, kulekanitsa chabwino ndi choipa. Mulungu apereke izo kwa ife, kuti ife tikhale ndi kulimbika kochita zimenezo.

<sup>74</sup> Tangoganizani chimene chikanati chikanachitika. Monga mmene ine ndimakuuzirani inu, ine ndikukhulupirira, mmawa uja, kapena ndinamumva winawake akunena izo, kuti pa... M' modzi wa wowonerera awa amene akuwonerera; ine ndaiwala chomwe inu mumawatchula iwo tsopano, pa bomba, kapena ndege zimene zikubwera. Osati pakale kwambiri, panali dongosolo linabwerapo kudzera kwinakwake, kuti iwo anayitanitsa midipiti yaikulu, yokhala ndi tindege tamabomba firii handiredi tokhala ndi mabomba a atomiki ndi mabomba a haidrojini akulendewera pansu pake.

<sup>75</sup> Osati pakale kwambiri, ku bwalo la ndege lalikululu mu Shreveport; m' modzi wa anyamata anatembenuka kumeneko mu misonkhano ya M'bale Jack. Iye anati, "Ife tiri ndi mabomba a atomiki akulendewera uko mu zopachikira."

Ine ndinati, "Kodi inu simuli . . ."

<sup>76</sup> "Mu. . ." Ine ndikutanthauza, "Mu—mu ndegezo; ndipo ife timakakwera ndi kumakayeserera ndi iwo, tsiku ndi tsiku."

Ine ndinati, "Kodi inu simumachita mantha?"

<sup>77</sup> Anati, "Izo ziribe zowomberera mwa izo. Koma ife tiri atcheru kwambiri, kuti mkati mwa danga la miniti, mphindi sikisite, ife tikhoza kukhala ndi zowombererazo mmenemo ndi kumapita. Ndi kuthiridwa mafuta ndi kukhala titakonzeka, iwo akhoza kuulukira ku England ndi izo, nthawi yomweyo."

<sup>78</sup> Zopachikira zazikuluzo zaikidwa uko mu nyanja za mchere, konsekonse. Ndipo iwo akumanena kwa Russia, "Uyerekeze kuponyera bomba limodzi! Ungoponyera bomba limodzi la atomiki pa U.N. kapena kwinakwake uko, ndipo uwone chomwe chiti chidzachitike!"

<sup>79</sup> Icho chidzakhala chiyani? Chidzakhala chiwembu chimene chidzapite kwa Russia. Ndipo ngati iwo angachite zimenezo, ndi kuyamba kuponya mabomba awo a atomiki ndi a haidrojini, izo zingayambitse kuwomberana kolumikiza kumene kukhoza kudzatentha dziko lapansi kukhala—ka nsalu, basi litangosungunuka. Inu mukudziwa, izo sizingatsutsane ndi Lemba mpang'ono pomwe. "Pakuti dziko lidzapsya, ndi kumwamba, nakonso." Ma atomu apa dziko lapansi adzapsya.

<sup>80</sup> Ife tikukhala mu tsiku lowopsya. Ife tikukhala mu tsiku limene anthu a mdziko akuiwopa imfa. Amuna otchuka, iwo—iwo akuchita mantha kuti ndani yemwe ati aphulitse bomba loyamba limenelo. Bomba loyamba limene liti liponyedwe, zikatero chinthu chonsecho chipita mu—mu kusonkhana.

<sup>81</sup> Iyo ikuyenera kukhala nthawi yokondweretsetsa mu dziko kwa Mkristu. Nthawi zidzasintha. Aakulu adzakhala aang'ono. Oh, mai! Imfa idzathawira kutali. Matenda sadzakhala ponso. Kopandanso misonkhano ya pemphero kwa odwala. Kopandanso misonkhano ya pemphero kwa otayika. Koma Mulungu adzabwera ndi kudzawatenga Osankhidwa kuchokera ku mphepo zinai za dziko lapansi, ndipo adzawasonkhanitsa iwo pansi pa phiko Lake lomwe, ndipo tidzakakhala ndi kukalamulira ndi Iye kwanthawizonse Kumwamba Kwake.

<sup>82</sup> Oh, m'bale, mlongo, mzanga wa ine, ngati sunakonzeke usikuuno, ukhale utakonzeka ora lino. Ine ndikukuitanira iwe kuti ubwere kwa Khristu Yesu, usikuuno, ndipo udzalandire. Inu amene mwakhala otsutsa, inu amene mukudziwa kuti inu simuli pamene inu mumayenera kukhala ndi Mulungu, ine ndikukuitanirani inu ku guwa ndi inemwini. Ine ndikuitanira mmodzi aliyense wa inu kuti mubwere kuno, ndipo osati kudzangonena, koma kuti mudzakhale pano kufikira Mulungu atatsuka moyo wanu kwa chirichonse chimene sichiri chofanana ndi Iye, mpaka kuti inu muchoke pano muli munthu watsopano. Osati mutavala chikhakha cha chimanga, koma kuchoka pano mutapatsidwa Magazi omwe amayeretsa magazi anu ndi kukupatsani inu Moyo watsopano ndi chiyembekezo chatsopano. Kuchokapo ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Kuchokapo, osati mukufuula, osati mukuvina, osati ndi zochuluka kwambiri. . . Zinthu zimenezo ndi zabwino. Zonsezo ndi za mu Tchalitchi. Zonsezo ndi za mu Baibulo. Koma chimene ine ndikuchikamba ndi Mzimu Woyera, chikondi cha Mulungu.

<sup>83</sup> Mnyamata wamng'ono amayankhulana nane tsiku lina. Amayi ake, mkazi wokondedwa. Ine ndamudziwa mkaziyo, ndinakumanapo naye kamodzi kapena kawiri. Ndipo iye anati, "Oh, wokondedwa," kwa mnyamata wake, "bwera kuno, ine ndikufuna kuti iwe uwone. Ine ndiri ndi mafuta mdzanja langa." Chabwino, ine ndiri nawo, inenso. Ndi kumene ndakhala ndikuchita thukuta. Tsopano, anati, "Ine ndiri ndi mafuta mdzanja langa." Anati, "Iwe ukuganiza chiyani za chimenecho?"

<sup>84</sup> Ndipo mnyamatayo anayang'ana pa amayi ake, ndipo anati, "Amayi, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake." Iwo ankafuna kuti iye apemphere, ankafuna kuti iye apemphere kuti iwo aziyenda pafupi ndi Mulungu. Iye anati, "Pamene mafuta anabwera mdzanja lanu, kodi iwo anachotsa kutsutsika kwanu konse? Kodi iwo anakupatsani inu chokuchitikirani chokoma ndi Mulungu, pamene mafuta. . ."

"Ayi."

Anati, "Ndiye ine ndingazisiye izo zokha." Ndi zimenezotu.

<sup>85</sup> Oh, dziko, dziko lachipembedzo, anthu achipentekoste, akufunafuna zopambana. Dziko, dziko (lotchedwa) lophunzira, dziko lachipembedzo, likufunafuna njira ina yapamwamba imene ikhoza kupambanitsa chipembedzo chawo ndi kutengera mamembala ambiri mmenemo, “ochuluka kupitirira milioni,” inu mukudziwa.

<sup>86</sup> Ndipo ma—mafuko akufunafuna mtundu winawake wa gulu la apolisi amene angalibweretse dziko lonse pa maondo ake, ndi kubweretsamo chirungamo.

<sup>87</sup> M’bale, izo sizimabwera mwa kupambana kwa chipentekoste. Ndiponso sizimabwera mwa mabungwe Achiprotestanti kapena mwa ufumu wolowezana wa Chikatolika. Ndiponso sizimabwera mwa mapentagoni, kapena kutsegula masamba atsopano. Izo zimabwera mwa moyo wogonjera kwa Yesu Khristu, kudzera mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Chirichonse chopelewerwa pa chimenecho, ndi cholakwika.

Tiyeni ife tipemphere.

<sup>88</sup> Ine ndimufunsa mlongo wathu kuti abwere pa limba pamenepo, piyano, pa nthawi ino. Pamene ife tiri mu pemphero, pamene munthu aliyense waweramitsa mutu wake, ndipo munthu aliyense ali mu pemphero. Ine ndikudabwa, pa mphindi ino, ngati inu mungapime mzimu wanu ndi Mawu a Mulungu. Kodi inu muli bwino?

<sup>89</sup> Chikatha chiyanjano chino, monga ine ndinakuuzirani inu. Ine ndiri ndi apongozi aakazi uko ali chigonere, ali pa nsonga kumene ya imfa. Ine ndiyenera kuti ndikawawone iwo. Iwo akufa. Azimzanga ena, amene ine ndikuwadziwa pano, amene ine ndikukawachezera, amene ali pa nsonga ya imfa, anthu amene anakhalapo mu tchalitchi chino. Oh, m’bale, mlongo, inu mukubwera kutsikira kumeneko, nanunso. Inu mukuyenera mudzafike kumeneko.

<sup>90</sup> Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, ine—ine ndikudziwa zimenezo, M’bale Branham. Ine ndikulinga kuti ndichikonze chinthu chimenecho, ena a masiku awa.” Koma mwina sizingakhale “ena a masiku awa,” kwa inu. Ili likhoza kukhala tsiku lokhalo.

<sup>91</sup> Munthu uja ankadziwa pang’ono bwanji, akubwera kuchokera ku California, akupita ku Michigan, tsiku lina, ali ndi mkazi wake wachichepere kuno, akuyendetsa ga—galimoto; iye ali mu piki-apu, akupita ku nyumba yawo yatsopano. Iye anali atangopuma kumene ntchito ya Usilikali wa panyanja. Iye ankadziwa motani pamene iye anali kunyamuka mmawa umenewo, mwinamwake akuchokera ku doko la alendo, kuti mkazi wake ndi khanda akhala mtembo mu maminiti ochepa? Koma, pamwamba chabe pa Henryville kumeneko, galimoto lawo linagundana ndi basi. Ndipo dalaivala anapangitsa ga—



ga...galimoto lake kumbuyo kupita kutsogolo, pafupifupi, koma ilo linamupha mkaziyo ndi mtsikana wamng'ono. Ine ndikudalira kuti moyo wawo unali bwino ndi Mulungu.

<sup>92</sup> Masabata pang'ono apitawo, pamene M'bale Wood ndi ine tinapita uko ku ndege imene inagwera kuseri kwa malo awa kuno, ndi kuwawona iwo akusolola zidutswa za matupi za amuna eyiti, pamene mitu ndi miyendo ndi mikono inali paliponse pa malopo. Akutola thupilo, ndipo ziwalo zamkati zikutulukira kunja kwa thupi la munthuyo; munthu wabwino, mwinamwake, munthu wotchuka wochokera ku Chicago. Pamene munthu ameneyo amalowa mu ndege m'mawa umenewo, ine ndikudabwa usiku umene iye anapita ku tchalitchi, ngati iye anali ndi zolinga zabwino. Kodi abusa anaitanira kuguwa? Kodi iwo anadzudzula tchimo, ndipo munthuyo anali ndi mwayi? Kapena kodi iye anapita uko ngati chinyama? Kodi munthuyo, pamaso pa Mulungu, anali mwana wa Mulungu?

<sup>93</sup> Taganizani za zinthu zimenezo, abwenzi. Izo ndi zofunikira. Izo si zofunikira kokha, izo ndi chinthu chofunikira kwambiri kwa inu ora lino. Ino ndi nthawi yomwe inu muti mupange chiganizo chanu. Ino ndi nthawi yomwe inu mungapange chigamulo chanu cha moyo uno, pa moyo winawo ukatha uno. Inu mungapange izo pamene ife tikupemphera.

<sup>94</sup> Atate Akumwamba, pamene ife tiwerenga mu Baibulo za zomwe Inu munanena za tchimo, ndi iwo amene amalichita ilo ndipo osalapa. Ife tikuzindikira chomwe izo chimatanthauza kufa opanda kumudziwa Mulungu. Ife tikudziwa izo mwa zowachitikira ena, amene ife tawawona akupita. Iwo amene ankafuna, iwo amene anazisunga izo nthawi yayitali. Mulungu, iwo amene ankavomereza ndipo osakhala nacho chimene iwo amati anali nachocho. Iwo amene anali kuchita ngati Akhristu, ndipo komabe iwo sanali Mkhristu. Moyu wawo umatsimikizira izo, ndipo imfa yawo inapangitsa kuti izo ziwonekere.

<sup>95</sup> Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu muyankhule kwa mtima uliwonse pano usikuuno. Ndi inemwini, Ambuye, pokhala wochedwachedwa, pa zinthu zambiri zomwe ndikanati ndichite ndipo sindinazichite, ine ndikuvomereza kulakwa kwanga. Ine ndikuvomereza zolakwa za anthu awa. Ine ndikuvomereza zolakwa za fuko lino. Ine ndikukupemphani Inu kuti mutichitire chifundo, Ambuye. Ine ndiri ndi ana atatu aang'ono uko oti ndiwalere. Ndipo ife tikukhala pano pamalo otentha, ndipo, Mulungu, palibe chifukwa chomathawira. Inu mukudziwa zonse za izi. Mulungu, ine ndikufuna kukhala woyanjala ndi Inu.

<sup>96</sup> Tsikulina, ngati bomba la atomiki silidzatitenga ife, ngozi idzatitenga. Ngati ngozi siidzatitenga ife, nthenda ina idzatitenga. Chinachake chikuyenera kudzatitenga ife.

Koma ndife okondwa kwambiri kudziwa kuti pali njira yopulumukirapo. “Dzina la Ambuye ndi—ndi nsanja, ndipo olungama amathawira m’menemo ndipo amakhala otetezeka.” Mulungu, mulole mzanga wochimwa, usikuuno, mnyamata, mtsikana, mwamuna kapena mkazi, awone khomo lotseguka, mwayi, ndipo athamangire kwa Khristu ora lino.

<sup>97</sup> Tsopano pamene mitu yathu ili yoweramitsidwa, kodi alipo ena pano, kapena adza . . . Ine ndikudziwa alipo ena pano amene akufuna kunena, ndi dzanja lokwezedwera kwa Mulungu, “Ine ndikuchita manyazi ndi moyo wanga. Ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndivomereze zolakwa zanga pamaso pa Mulungu, ndi kupempha chifundo.” Kwezani mmwamba dzanja lanu kwa Mulungu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Alipo ambiri a inu, ambiri a inu. Eya. Alipo ambiri a inu pano, inunso, amene . . . Mulungu akudalitseni inu.

<sup>98</sup> Ambiri a inu pano, amene mwadzinenera Chikhristu kwa nthawi yaitali, ndipo mukudziwa kuti inu mwalephera kuti mukoke chingwe cha Mulungu, mukudziwa kuti mukuchita zinthu pakali pano zimene inu simumayenera kuti muzichita. Ndipo inu mukumapita, osazilapa izo, momasuka mukumangoyandama nalo fundelo. Kumawonera maprogramu amene inu simukuyenera kumayang’anapo. Kumayang’ana mtundu wa magazini ndi kumawerenga mabuku amene inu simukuyenera kuwerenga. Ndi zosayenera kwa Mkhristu. Kumvetsera nthabwala zoipa—zoipa ndi zonyasa ndi za mwaye zomwe inu mukudziwa kuti simukuyenera kuti muzichita; onse awiri amuna ndi akazi. Inu mukudziwa za malo amene inu mukanakayankhula ndipo inu simunakachite izo, ndipo inu muli olakwa, mwinamwake, tchimo la kusachita.

<sup>99</sup> Ine ndikudabwa ngati inu mungakweze dzanja lanu kwa Khristu, kuti akuchitireni inu chifundo, ndipo akukhululukireni inu. Kwezani dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono; pamene mkaziyo akuyenda, kuti abwere ku guwa, kuti adzalape zake. Kwezerani dzanja lanu kwa Mulungu. Mulungu akudalitseni inu. Ndiko kulondola, bambo. Uko nkulondola. Mulungu akudalitseni inu. Kwezani dzanja lanu. Inu mukudziwa mwachita cholakwika.

<sup>100</sup> Ine ndikudabwa ngati muli ndi kulimbika, usikuuno, kuti mukumane nane pano pa guwa. Tiyeni tigwade mozungulira pano ndi kuti, “Mulungu, chitirani chifundo kwa tonse a ife. Ife tikukusowani Inu.” Mulungu akudalitseni inu, dona.

<sup>101</sup> Kuwawona akazi aang’ono awa akubwera, akulira, moyo uli patsogolo pawo! Iwo ali pa mphambano. Iwo ndi ogwidwa mu zochitika. Chiyani? Kodi inu mukuzindikira, azibambo, pamene ife tinali anyamata, anyamata athu ali ndi kuchulukitsa ka teni mayesero amene ife tinkakhala nawo? Mlongo, kodi inu

mukuzindikira kuti mwana wanu wamkazi ali ndi kuchulukitsa ka teni mayesero amene inu munkakhala nawo pamene inu munali mtsikana? Kodi mwana wake wamkazi adzakhala ndi chiyani? Tayang'anani pa zinthu, zithunzi zimene mdierekezi akujambula.

<sup>102</sup> Oh, mmene ife tikusowekepera kupemphera! Tsopano ife tibwereranso kwa inu kachiwiri. M'bale, kodi inu mukuzindikira kuti ife sitikupemphera theka la momwe atate athu ankachitira? Abusa, kodi inu mukuziwa kuti ife sitikuika nthawi yochuluka pa maondo athu monga azibusa ammbuyo mwathu ankachitira? Akazi, kodi inu mukuzindikira kuti inu simumamulangiza mwana wanu wamkazi, ndi kupemphera naye usiku, monga m'mene amayi anu ankachitira nanu inu? Ndiye, nanga bwanji zimenezo, wolakwa ndi ndani? Ife tiri olakwa. Palibe njira iliyonse yozembera izo. Ife tiri olakwa.

<sup>103</sup> Ndine wolakwa. Ndine wolakwa pa kusagwira ntchito ya Mulungu, monga ine ndikuyenera kuchitira. Ine ndikuvomereza izo, kuti ndine wolakwa. Ine ndikumupempha Mulungu kuti andichitire ine chifundo. Ine ndimayang'ana kunja uko ndi kuwona mwayi imene ine ndaiphonya, chifukwa cha zinthu zopanda pake, zazing'ono, zinthu zakale zosafunikira zimene sizimatanthauza chirichonse. Ine ndikuzichitira manyazi inemwini, ngati mtumiki wa Uthenga pamaso panu. Ine ndikulapa pamaso pa Mulungu, ndipo ndikumupempha Mulungu kuti andikhululukire ine, ndi mpingo undikhulukire ine, pokhala wochedwachedwa pa ntchito ya Mulungu. Mwa chisomo cha Mulungu, ndi mothandizidwa ndi Mulungu, ine sindidza—ine sindidzamvetsera ku chimene... Aliyense akuyesera kukuuzani inu chinachake choti muchite. Iwo ali ndi dongosolo. Iwo ali ndi chinachake choti inu muchite. Zamkhutu. Ine ndikuziwa dongosolo la Mulungu; ilo linalembedwa umu mu Baibulo. Ndipo ine ndikuzichitira manyazi inemwini ngati mtumiki wa Uthenga. Miyoyo wani milioni yapindulidwa; ine ndimayenera kupindula miyoyo teni milioni. Ine ndatsalira mmbuyo kutali.

<sup>104</sup> Nanga bwanji inu? Ndi miyoyo ingati yomwe inu mwaipindula chikhalireni mwa Khristu? Chikhristu chimangoyenda kuchoka kwa wina kupita kwa wina. Ndi miyoyo ingati imene inu mwaipindula chikhalireni Mkhristu? Ngati inu simukupindula miyoyo, inu ndi wolakwa, inu ndi wosabala, inu mwabweretsa manyazi pa Mpingo ndi Uthenga. Ndi anthu angati amene inu mumawafikira pa msokhano wa mapemphero wa Lachitatu usiku? Ngati inu simukuchita zimenezo, inu muyenera kudzichitira nokha manyazi pamaso pa Khristu. Ndinu wolakwa, ndipo malo anu ndi pa guwa. Ine ndikukuitanani inu kuti mubwere ndi ine, kuti mudzalape. [M'bale Branham akuimikira—Mkonzi.]

<sup>105</sup> Ndiye kodi inu mungaweramitse pansu mitu yanu, ndi kuisiya iyo yowerama kwa miniti, pamene ine ndikumverera kulakwa kwanga ndipo ndikufuna kuti ndilape. Ingoweramitsani mutu wanu. [M'bale Branham akuchoka pa gome ndipo akukagwada pa guwa—Mkonzi.]

<sup>106</sup> Atate athu Akumwamba, ine ndikuwerama pa guwa ili ndi kupempha chikhululukiro pa tchimo langa. Ine ndikupempha chikhululukiro cha machimo a iwo amene ali mozungulira guwali. Ine ndikupempha chikhululukiro cha mpingo uwu, pa thupi—pa thupi la okhulupirira fuko lonse ndi konsekonse. Ine ndikupempha chifundo pa ife, pokhala ochedwa kwambiri pa zinthu zokhudza Ufumu. Ine ndikupempha kuti Inu mutikhululukire ife machimo athu, ndipo muchotse za—za—mphulupulu zathu. Ndipo mutikhululukire ife chifukwa chokhala opusa kwambiri, chifukwa cha kupusa kwa anthu. M'mene ife taperewerera! M'mene ife tatengera kuchitachita kwa thupi! M'mene ife tachitira zinthu zimene ife sitimayenera kuti tizichite! M'mene ife tachimwira pamaso Panu!

<sup>107</sup> Ndipo pa msonkhano wa usiku wa Lamlungu uno, Atate, powona mneneri wochita manyazi wa Baibulo, ife tikuchita manyazi usikuuno. Ine ndikuchita manyazi pamaso Panu, chifukwa cha machimo a anthu. Anthu, fuko langa, anthu anga, ine ndachititsidwa manyazi chifukwa cha iwo, Ambuye. Kuwona akazi athu aang'ono akuyenda mmisewu ndi kumachita m'mene iwo akuchitira! Kuwona uchisembwele, anyamata kumakhala mu—mu mitundu yonse ya moyo! Kuwawona iwo akukhala ku nyumba osapita ku tchalitchi, ndi kumawerenga magazini akale omwe iwo sakuyenera kuwerenga! Kumawonela maprogramu osasefedwa! Kumamvetsera nthabwala zonyansa za ku Hollywood! Kumamvetsera nyimbo za gwedemula za mdierekezi, zimene zakonkhomoledwa kuchokera kwa amuna a mbiri yoipa ndi okhala ndi chikumbumtima choipa, chikoka cha mdierekezi, kuti chikadzodze ntchito za mdierekezi!

<sup>108</sup> O Mulungu, ndine wamanyazi inemwini chifukwa chosadzudzula mwanjira imene ine ndimayenera. O Mulungu, chotsanipo kulakwa kwanga. Ine ndikukupemphani Inu kuti muchite zimenezo. Ine ndikupempha kuti Inu muwakhululukire anthu awa amene ali pano, poyamba, ife tonse. Tithandizeni ife kuti tidzuke kuchokera pa guwa ili amuna ndi akazi atsopano. Tithandizeni ife kuti tipite kuchokera pano monga Akhristu ayenera kupitira.

<sup>109</sup> Tithandizeni ife kuti “Tikaike kumbali kulemera kulikonse, ndi tchimo limene silimachedwa kutifooketsa ife, kuti tikathe kuthamanga ndi chipiriro liwiro limene layikidwa patsogolo pathu.” Osati kuyang'ana kwa televizioni, osati kuyang'ana kwa anthabwala a mdziko, koma, “Kuyang'ana kwa Woyambitsa ndi Womalizitsa wa chikhulupiriro chathu, Ambuye Yesu Khristu, Yemwe ananyoza manyazi a mtanda ndi kuwunyamula iwo

chifukwa cha ife, ndipo anazunzika kunja kwa chipata, kuti Iye akathe kuwayeretsa anthu ndi Magazi Ake.”

<sup>110</sup> Titsukeni ife ku kusalungama konse, ndipo mutitenge ife ngati ana Anu omwe, usikuuno, ndipo mutilandire ife mu pemphero ili la kulapa. Ndipo mutipatse ife, Ambuye, mtendere ndi chimwemwe. Ndipo mukalole mabedi onse, usikuuno, pamene ife tizikagona, tikuganiza za msonkhano wa usikuuno, mulole ife tizikaganizira za zikhaliidwe za mdziko, zimene Baibulo lawulula kwa ife tsopano. Mulole ife, pamene ife tizikaganizira za izo, nkhope zathu zikakanthidwe ndi manyazi, ndipo Inu mukabweretse mtendere ndi chimwemwe kwa mtima uliwonse. Ife tikulapa, Ambuye, pamaso Panu, pa guwa ili.

<sup>111</sup> Mulungu, ndithandizeni ine pamene ine ndikupita tsopano, mwa chikhulupiriro, ndi kupemphera kuti izi zikhale mu chifuniro Chanu, kuti ambiri, ambiri, mazana ambiri a anthu akakhoze kupindulidwira kwa Inu. Ndipo mundithandize ine kukhala ndi chikhulupiriro ndi kulimbamtima, pamene ine ndizikapitirira; osati kuyang’ana kwa aliyense koma kwa Inu, Woyambitsa ndi Womalizitsa wa chikhulupiriro chathu. Mulungu, perekani izi.

<sup>112</sup> Mumukhululukire dikoni aliyense wa mpingo uno. Akhululukireni abusa. Muwakhululukire mamembala wamba, Ambuye. Mukhululukire aliyense a machimo athu. Tikhululukireni ife, Ambuye. Mumukhululukire mlendo aliyense pa chipata chathu. Ndipo mulole ife timverere kukhudza kwa Mzimu Woyera pa moyo wathu, chifukwa ife tadzichepetsera pamaso Panu, usikuuno, kulapa ndi mtima wathu wonse, kuti Inu mutilandire ife ndipo mutipange ife odzichepetsa, ofatsa, oyeretsedwa, anthu odzichepetsera ku ntchito Yanu. Perekani mdalitso uwu, Ambuye, pa guwa pamene ife tilipo. Perekani izi. Ndipo tikuweramitsa mutu wathu ndi mitima yathu pamaso Panu. Mu Dzina la Mwana Wanu, Ambuye Yesu, ife tikupempha izi. Amen, ndi Amen.

Ndine Wanu, O Ambuye, ndamva liwu Lanu,  
Ndipo landiiza chikondi Chanu kwa ine;  
Ndi motani ndifunitsa kukwera m’manja a  
chikhulupiriro,

Ndi kukokedwa moyandikira kwa Inu.

Ndisendeze mfupi, mfupi, Ambuye wodala,  
Ku mtanda kumene Inu munaferako;  
Ndisendeze mfupi, mfupi, mfupi, Ambuye  
wodala,

Ku mbali Yanu yofunika, yowukha magari.

<sup>113</sup> Cha paguwa, usikuuno, pakati pa abale anga amene ali kuno pa guwa, ndine wokondwa kuwona, usikuuno, zam’mene amuna aliri ochuluka monga aliri akazi. Kawirikawiri, ndi akazi amene amasweka mophweka. Mitima yawo, pali chinachake chokhudza

iwo, amakhoza kukhudzika mophweka chifukwa cha ukazi. Ndipo iwo ali—iwo ali madona, ndipo iwe nthawizina ukhoza kuwakhudza iwo. Koma ndine wokondwa kwambiri kuwona Mzimu Woyera wakhoza kuwakhudza amuna, nawonso, ndipo wawabweretsa iwo pa guwa.

<sup>114</sup> Ndipo ine ndikudabwa ndi angati a inu amene muli pa guwa, amene mwagwada tsopano, amene mukumverera kuti mwapanga kudzipatulira kwa Mulungu, kuti inu mukuchoka pano usikuuno, kukakhala moyo wabwinoko, mwa chisomo cha Mulungu, ndi kukachita zochuluka kwa Ufumu wa Mulungu, ndi kwa cholinga Chake. Kodi inu mungakweze dzanja lanu kwa Khristu, ngati inu muli pano paguwa, nenani, “Ine ndikukhulupirira kuti tsopano ine ndalapa.” Ambuye akudalitseni inu.

<sup>115</sup> Ndi angati a inu kumbuyo uko mukumverera kuti inu mwalapa mutakhala pa mpando wanu; mukumverera ngati kuti mukufuna kuchita bwino? Mulungu akudalitseni inu.

Tsopano tiyeni ife tiime.

<sup>116</sup> Inu pano pa guwa, muyang’ane mbali *iyoyi*, ngati inu mungatero. Tsopano, inu kuno pa guwa, kwezani manja anu kumeneko, kuti inu mukukhumba pemphero lawo, kuti inu mukhoze kumapitirirabe. Mungakwezere manja anu kwa iwo amene ali kwa omvetsera? Chabwino. Tsopano inu mukweze manja anu kumbuyo kuno, pa guwa kuno, kuti inu mukukhumba pemphero lawo, nanunso. Kuti ife. . . Mulungu atithandize ife kuti titero. Ambuye Yesu atidalitse ife.

Tsopano, musaiwale chiyanjano cha Lamlungu usiku.

<sup>117</sup> Kodi inu muli ndi mawu oti munene, M’bale Neville? [M’bale Neville akuyankhula kwa M’bale Branham—Mkonzi.] Lachiwiri ndi Lachitatu usiku. . . Kodi mishoni imeneyo ili kuti? [M’bale Neville akuyankha.] 1628 West Market, Lachiwiri likubwerali ndi Lachitatu usiku.

<sup>118</sup> Ndipo kenako Loweruka ndi Lamlungu, ine ndidzakakhala ku Madisonville, Kentucky, ku nyumba yolankhuliramo kumeneko. Ndipo kenako ife tizidzapita ku New York.

<sup>119</sup> Tsopano, chifukwa chimene ife tikuchoka molawirirapo, ine ndiri ndi apongozi anga aakazi amene ali, akudwala kwambiri, ndipo iwo akundiitanitsa ine. Tsopano tiyeni ife. . .

<sup>120</sup> Muli ndi mawu oti munene, M’bale Neville? [M’bale Neville akuti, “Ayi.”—Mkonzi.] Ndiribe.

<sup>121</sup> Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kwa kamphindi chabe, pamene ife tikupemphera. Chabwino. Pang’ono pang’ono tsopano:

Mulungu akhale nanu mpaka tidzawonanenso!

Mwa. . .



*MNENERI WOCHITA MANYAZI* CHA56-1125E  
(A Blushing Prophet)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham unalalikiidwa mu Chingerezi Lamlungu usiku, Novembala 25, 1956, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mu chaka cha . . . ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2018 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)